EXAMINATION NO.:________________________

# DOWA DISTRICT EXAMINATIONS BOARD

## 2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK

## CHICHEWA

(Malikisi 100)

**(LA MASO AKULU)**

**Subject Number: P032**

**Nthawi: 2 h, 15 mins**

**Dzina lanu** : ____________________________________________
(*kuyamba ndi la bambo*)

**Dzina sukulu**: ____________________________________________

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba khumi ndi awiri.**
2. Pepalali lili ndi magawo anayi**:** Gawo **A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani **dzina lanu** pamwamba pa tsamba lilironse.
4. Yankhani funso limodzi lokha mu ngawo **A** pa mpata omwe mwapatsidwa, ndi kuyankha
mafunso onse mu gawo **B**, **C** ndi **D**.
5. Mgawo **B** ndi **C**, lembani mayankho anu m'mipata yomwe mwapatsidwa pa pepalali**.**
6. Yankhani mafunso anu mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza pa funso lililonse.
7. Muchitebulo chili pa mwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mu bokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
8. Perekani pepalali kwa **oyang'anira** nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-22 | | | |
| 23-25 | | | |
| 26-28 | | | |
| 29-31 | | | |
| 32-33 | | | |
| 34-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

**MUSAGWIRE PEPALALI MUSANAUZIDWE NDI OYANG'ANIRA**

**© 2024 DOWA**

**Onani Paseri/…**

**Gawo A** (Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso **limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo **kapena** kalata. Mawu achimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150**.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu awu **"NJINGA YOMWE INASOWA",**

Mwazina tsatani izi polemba;

**Ndime yoyamba**
- Lidali tsiku liti lomwe njingayo idasowa
- Komwe mudali patsikuli

**Ndime yachiwiri**
- Njingayo idali yamoto kapena yakapalasa
- Mudachitapo chiyani njingayo itasowa
- Tchulani anthu awiri omwe anakuthandizani

**Ndime yachitatu**
- Nenani ngati njingayo inapezeka
- Anthu omwe adabawo munachita nawo chiyani ngati adapezeka

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa mkulu wanu yemwe mumakhala naye mukapanga tchuthi ku sukulu yomupempha kupita kunyanja paulendo womwe sukulu yanu yawupanga.

Mwa zina tsatani izi polemba;

**Ndime yoyamba**
- Cholinga cha kalata
- Dzina la Nyanja yomwe mudzapite
- Tsiku la ulendo
- Kuchuluka kwa ndalamazo

**Ndime yachiwiri**
- Zomwe mukuyembekezera kukawona
- Kufunika kwa ulendowo pamaphunziro anu

**Ndime yachitatu**
- Chisangalalo chomwe mudzakhale nacho mukadzapita nawo ku ulendowo

Tsamba loyankholapo

Mafunso akupitirira…

## Gawo B (20 Marks)

**3.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenako yankhani mafuso otsatirawa

Kalekale dziko likadali mphonje, kudali nkhalango yowirira kwambiri yotchedwa Nkhufi. Nthaka ya m'nkhalangomo idali yachonde ndipo msipu udali ponseponse. M'nkhalangomu mudali mitengo ya chilengedwe ndi nyama zambiri. Mfumu ya m'nkhalangomo idali Mkango ndipo nduma zake zidali Njati, Mvuu, Nyamalikiti, Chipembere, Nchefu ndi Njobvu. Nyama zonse zomwe ndi zolusa kwa anthu masiku ano, kalelo zidali zosaopsa.

Mkango ndi nduna zake zimamwa madzi mnyanja pomwe nyama zazing'onozing'ono zimamwa madzi a m'mitsinje popereka ulemu kwa akuluakulu awo. Pa nyama zonse zazing'onozing'ono, Kalulu yenkha ndiye amayandikira kwa akuluakulu aja chifukwa cha ukavuwevuwe ndi umbava. Kalulu adalinso ndipsi. Iye amakonda kuba mtedza m'zilere za anzake. Pofuna kudziteteza akapalamula, iye amakonda kutumikira kunyumba kwa mfumu.

Masiku ena nyamazi zimakhala mwamantha chifukwa cha anthu omwe amakonda kuchita uzimba m'nkhalango. Tsiku lina mfumu Mkango idaitanitsa nduna zake kuti akakambirane njira zodzitetezera kwa adani awo chifukwa miyoyo yawo idali pa chiopsezo chachikulu. Mfumu ndi nduna zake zisadakumane, Kalulu adali atamva kale za nkhaniyo. Iye adanamiza Mkango kuti agogo ake adamuphunzitsa using'anga ndipo atatsilika nkhalangoyo palibe yemwe adakatha kutsilikula. Mfumu Mkango idamukhulupilira Kalulu chifukwa kalekalelo kudali Kalulu wina wokhwima kwambiri.

Mfumu itamva za nzeru ya Kalulu idadziwitsa nduna zake nkhaniyo pamene amakambirana za chitetezo. Nduna zina zidakhulupilira koma Chipembere, Ntchefu ndi Njovu zidachenjeza anzawo kuti adayenera kusamala ndi Kalulu chifukwa adali pakomeine. Padaoneka kuti nduna zija zidasemphana Chichewa ndipo zidayamba kupsetsana mitima. Mfumu idalowerelapo ndi kuziyanjanitsa. Posafuna kukhumudwitsa mfumu, Chipembere, Ntchefu ndi Njovu zidagwirizananso kuti Kalulu uja akadzawapusitsa adzamupatse chilango choopsa.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa:**

**a.** Tchulani zinthu **ziwiri** zomwe zidali m'nkhalango ya Nkhufi?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**b.** N'chifukwa chiyani nyama zazing'onozing'ono zimamwa madzi m'mitsinje mokha osati m'nyanja?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**c.** Kalulu amakonda kutumikira kunyumba kwa mfumu chifukwa chiyani?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**d.** N'chifukwa chiyani nyama zimakhala mwamantha m'nkhalango muja masiku ena?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**e.** Perekani matanthauzo a mawu awa monga momwe awagwiritsira ntchito m'nkhaniyi?

**i.** Wokhwima

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**ii.** Pakomeine

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**f.** N'chifukwa chiyani mfumu Mkango idamukhulupilira Kalulu kuti atha kutsirika nkhalango?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**g.** Tchulani nduna **ziwiri** zokha zomwe zidakhulupilira kotheratu pa mawu a Kalulu woti atha kutsilika nkhalango?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**h.** Pezani mawu mu nkhaniyi omwe akutanthauza izi;

**i.** Palamula

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**ii.** Thetsa mphamvu ya mankhwala otsirikira zinthu

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**i.** Fotokozani zomwe nduna za amfumu zidagwirizana kudzachita ngati Kalulu adzawapusitsi?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

**j.** Perekani mutu wa nkhaniyi?

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

## GAWO C (10 MALIKISI)

Yankhani mafuso onse **awiri** m'gawoli

**4.** Werengani kankhnika ndipo kenako muyankhe mafuso otsatirawa

*A Chibwe: Chavuta n'chiyani bamboo?*
*A Mafuta: Thupi lonseli likuphwanya kwambiri komanso ndikuchita chizungulire*
*A Chibwe: Chabwino. Gonani apa kuti ndikupimeni*

**Mafuso**

**a. i)** Kodi ndi malonje anji amenewa?

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**ii)** Malonjewa akuchitikira kuti

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**iii)** Kodi a Chibwe ndi ndani mnkhaniyi

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**b. i)** Perekani njira **imodzi** yotumizira uthenga wa ukwati

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

**ii)** Kodi getsi lofiira limasonyeza chiyani pa nsewu

_______________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu otsatirawa kusonyeza kuti mukudziwa matanthauzo ake

a. mbulanda

________________________________________

________________________________________ **(malikisi 1)**

b. zakuda

________________________________________

________________________________________ **(malikisi 1)**

c. namwino

________________________________________

________________________________________ **(malikisi 1)**

d. kwa

________________________________________

________________________________________ **(malikisi 1)**

e. mwaulemu

________________________________________

________________________________________ **(malikisi 1)**

## Gawo D (40 Malikisi)

**Mafunso 6 mpaka 10.** Sankhani mitundu **(A, B, C** kapena **D)** ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

6. Mwana ali <u>gone</u> m'nyumba.
   - **A.** Mfumu
   - **B.** Mfotokozi
   - **C.** Mneni
   - **D.** Mvekero

7. Ndikufunira <u>kuchira</u> mwamsanga.
   - **A.** Dzina
   - **B.** Mfotokonzi
   - **C.** Mneni
   - **D.** Mlowam'malo

8. <u>Ngakhale</u> mukundiletsa ndipitabe kusukulu.
   - **A.** Mfotokozi
   - **B.** Mlumikizi
   - **C.** Muonjezi
   - **D.** Mneni

9. <u>Mwaba</u> mabuku anga.
   - **A.** Dzina
   - **B.** Mfotokozi
   - **C.** Muonje
   - **D.** Mneni

10. Jonasi wagula nzimbe <u>ziwiri</u>.
   - **A.** Mfotokozi
   - **B.** Muonjezi
   - **C.** Mvekero
   - **D.** Dzina

**Mafunso 11 mpaka 15,** Sankhani mitundu **(A, B, C** kapena **D)** ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

**11.** Eee, ndiwozi ndi zokomadi.

**A.** Okana
**B.** Otsindika
**C.** Ovomera
**D.** Othokoza

**12.** Upita liti kusukulu?

**A.** Wanthawi
**B.** Ofunsa
**C.** Owerenga
**D.** Oloza

**13.** Ndakhuta kwabasi nsimayi.

**A.** Owerengera
**B.** Otsindika
**C.** Othokoza
**D.** Wa muyeso

**14.** Amayi adafika bwino.

**A.** Wamchitidwe
**B.** Wa nthawi
**C.** Wovomera
**D.** Wofotokoza

**15.** Tuluka m'khola la mbuzi.

**A.** Ovomera
**B.** Wa malo
**C.** Wa dzina
**D.** Otsimikiza

**Mafunso 16 mpaka 17.** Sankhani nthawi **(A, B, C** kapena **D)** za aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

**16.** Bambo uja amathamanga kwambiri.

**A.** Yamtsogolo
**B.** Yakale
**C.** Yanthayi
**D.** Yakawirikawiri

**17.** Boma lidalengeza zotsatira za mayeso.

**A.** Yatsopano
**B.** Yamtsogolo
**C.** Yakale
**D.** Yakale yathayi.

**Mafunso 18 mpaka 22.** Sankhani ntchito **(A, B, C** kapena **D)** za mitundu ya alumikizi yomwe yatsekedwa mizere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

**18.** Sindibwera ku ntchito chifukwa ndadwala.

**A.** Wopenekera
**B.** Wazotsatira
**C.** Wa chifukwa
**D.** Wa cholinga

**19.** Sankawerenga choncho walephera mayeso

**A.** Wosiyanitsa
**B.** Wopeneka
**C.** Wazotsatira
**D.** Wachifukwa

**20.** Muyenera kumulangiza <u>osati</u> kumumenya
- **A.** Wolekanitsa
- **B.** Wopeneka
- **C.** Wachifukwa
- **D.** Wa pokhapokha

**21.** Timugulire Malaya <u>kapena</u> nsapato.
- **A.** Wophatikiza
- **B.** Wapokhapokha
- **C.** Wopeneka
- **D.** Wachifukwa

**22.** Tikulandira mbewu <u>kuti</u> tikadzale kudimba.
- **A.** Wacholinga
- **B.** Wolekanitsa
- **C.** Wopenekera
- **D.** Wachifukwa

**Mafunso 23 mpaka 27,** Sankhani chachikazi cha mawu awa omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**23.** <u>Muphwa</u> wamenyedwa dzuro.
- **A.** Mkwati
- **B.** Mfumakazi
- **C.** Mferakazi
- **D.** Chipsolopsolo

**24.** Kwathu kuli <u>tambala</u>.
- **A.** Msoti
- **B.** Thadzi
- **C.** Chipsolopsolo
- **D.** Mwanapiye

**25.** <u>Muna</u> uja wabwera lero
- **A.** Mnyamata
- **B.** Mbombe
- **C.** Zakhali
- **D.** Mkazi

**26.** Dzana ndinaona <u>nthendo</u>.
- **A.** Kalulu
- **B.** Thadzi
- **C.** Vumbwe
- **D.** Ntchowa

**27.** Kwathu tidyera <u>mzambwe</u>.
- **A.** Thadzi
- **B.** Mthoni
- **C.** Nkhunda
- **D.** Mkota

**Mafunso 28** mpaka **30**, Sankhani chiganizo **(A, B, C** kapena **D)** chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za mkalembedwe mziganizo zotsatirazi.

**28.**
- **A.** Mwatenganji m’dengumo?
- **B.** Mwatenganji mdengumo?
- **C.** Mwatenganji m’dengumo.
- **D.** mwatenganji m’dengumo?

**29.**
- **A.** Haa! Mwana watentha khumbi lija?
- **B.** Haa! Mwana watentha khumbi lija.
- **C.** Haa! mwana watentha khumbi lija.
- **D.** Haa!, Mwana watentha khumbi lija!

**30.A.** Ndipatse mtedza, Adatero Jenifa.
**B.** Ndipatse mtedza, "Adatero Jenifa."
**C.** "Ndipatse mtedza," Adatero Jenifa.
**D.** "Ndipatse mtedza, "adatero Jenifa.

**Mafunso 31 mpaka 33,** Sankhani ntchito **(A, B, C** kapena **D)** za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

**31.**Melise, thawa kubwera chilombo.
**A.** Mwininkhani
**B.** Pamtherankhani
**C.** Lapadera
**D.** Loyitanira

**32.**Timamwa mkaka kuchokera ku ng'ombe.
**A.** Mwininkhani
**B.** Panntherankhani
**C.** Losonyeza malo
**D.** Lapadera

**33.**Amayi ndi abambo adapita ku Zomba.
**A.** Losonyeza malo
**B.** Mwininkhani
**C.** Lapadera
**D.** Pantherankhani

**34.**Jabesi mbiyang'ambe wamwalira.
**A.** Pamtherankhani
**B.** Mwininkhani
**C.** Loyitanira
**D.** Lapadera

**35.**Khoswe waphedwa ndi mphaka.
**A.** Mwininkhani
**B.** Pantherankhaini
**C.** Loyitanira
**D.** Losonyeza malo

**Mafunso 36 mpaka 38,** Sankhani mikuluwiko yotsutsana m'matanthauzo **(A, B, C** kapena **D)** ndi yomwe mwapatsidwa mziganizo zotsatirazi.

**36.**M'phechepeche mwa njovu sapitamo kawiri
**A.** Chibwereza chidaphetsa kunda
**B.** Bza sapita kawiri
**C.** Mphini zobwereza ndi zomwe zimatumba
**D.** Mapanga awiri avumbwitsa

**37.**Pakadafunda padajiwitsa galu.
**A.** Kuona maso a nkhomo n'kudekha
**B.** Zengerezu adalinda kwawukwawu.
**C.** Ndapakonda adasiya m'khonde
**D.** Ndionetsetse adathetsa nkhosa

**38.**Tinkanena anthera msiizi
**A.** Mawu a akulu akoma akagonera
**B.** Tsabola wakale Sawawa
**C.** Akuluakulu ndi mdambo mozimira moto
**D.** Likaomba wotheratu

**Mafunso 39 mpaka 40,** Sankhani Chichewa **(A, B, C** kapena **D)** choyenera cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**39.** Mnyamata uja wavaya kusukulu.

- **A.** Wapita
- **B.** Wabwera
- **C.** Akuyenda
- **D.** Watenga

**40.** Masiteni ake abwera lero.

- **A.** Abambo
- **B.** Amayi
- **C.** Azakhali
- **D.** A chemwali

**Mafunso 41 mpaka 45,** Sankhani mtundu **(A, B, C** kapena **D)** wa nthambi ya chiganizo chomwe chili ndi mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi.

**41.** Adawapeza pamene ali mtulo.

- **A.** Ya dzina
- **B.** Ya muonjezi
- **C.** Ya mfotokozi
- **D.** Yoyima payonkha

**42.** Mupatseni nsima kuti aleke kulira.

- **A.** Ya dzina
- **B.** Ya muonjezi
- **C.** Ya mfotokozi
- **D.** Yoyima payonkha

**43.** Kuti ndinu mwana ndizoona.

- **A.** Ya muonjezi
- **B.** Ya dzina
- **C.** Yoyima payonkha
- **D.** Yamfotokozi

**44.** Mtsikana amene wakhala apoyo ndi wamwano.

- **A.** Ya dzina
- **B.** Ya muonjezi
- **C.** Ya mfotokozi
- **D.** Yoyima payokha

**45.** Muuzeni avine monga akudziwira.

- **A.** Ya dzina
- **B.** Ya muonjezi
- **C.** Ya mfotokozi
- **D.** Yoyima payokha

## MAFUNSO ATHERA APA!!!

**NB: Pepala ili liri ndi masamba khumi ndi awiri osindikizidwa**